

**Danieli : 7:13-23**

**Mutu : Tanthauzo la zirombo zinayi**

Ndipereka moni kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau a Mulungu opezeka pa Masalmo 30:5, momwe Mulungu akuti, “Pakuti mkwiyo wake ukhala kanthawi kokha; koma kuyanja kwake moyo wonse.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kukambirana pa Danieli 7:7-13, m’mene timakambirana nkhanu ya nyangayaying’ono ndi mwana wamunthu. Ndipo lero mu Danieli 7:13-23, tiunika za tanthauzo la zirombo zinayi.

13.Ndinaona m’masomphenya a usiku, taonani anadza ndi mitambo ya Kumwamba wina ngati mwana wa munthu, nafika kwa nkhalamba ya kale lomwe; ndipo anamyandikizitsa pamaso pake.

Tsono Danieli sakuona zizindikiro monga za nyama zija ayi, koma akuona kukhazikitsidwa kwa ufumu wa Mesiya ndi woyera mtima wonse. Ndipo taonani Danieli akuti anaona mwana wa munthu, dzina lomwe m’Chipangano Chatsopano, Ambuye Yesu

akudzitanira. Uwu, ndiwo udindo womwe Mesiya adzagwiritsa ntchito poonongachirombochachinayinalandira mphamvu ndi ulamuliro wa Iye mwini, mwakupatsidwa ndi Atate wake kukhala Mfumu ya mafumu onse.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa pano kuti, Ambuye wathu Yesu Kristu ndiye mwalawosemedwa wopanda manja, umene udzathyola fano kunena kuti choipa china chilichonse, nadzakhazikitsa ufumu wake pansi pano. Kutsimikiza mau apa Masalmo 2:9, akuti, “Udzawathyola ndi ndodo yachitsulo; udzawaphwanya monga mbiya ya woumba.” Kutsindika kuti pamene Mesiya akubwera kachiwiri, ufumu wa satana, udzathyoka ndi onse womuukira Iye ndipo onse womvera Iye, adzalowa mu Ufumu wake. Kodi inu mwakonzekera kulowa mu Ufumu umenewu?

14.Ndipo anampatsa ulamuliro, ndi ulemerero ndi ufumu kuti anthu onse ndi mitundu yonse ya anthu ndi a manenedwe onse amtumikire; ulamuliro wake ndi ulamuliro wosathawosapitirira, ndi ufumu wake sudzaonongeka.

Pano Ambuye wathu Yesu Kristu akuonetsedwa kuti ndiye wamphamvu yonse pansi pano. Taonani pamene anakakhala ndi Atate, anatenga mphamvu zonse pa ana a anthu monga mwa mau apa Yohane 17:2, pamene akuti, “Monga mwampatsa Iye ulamuliro pa thupi liri lonse, kuti onse amene mwampatsa Iye, awapatse iwo moyo wosatha.” Tsono ndi mau awa, ndikuthakuona kuti Danieli ndi anzake akuthunzitsidwa mitima yawo, chifukwa akuona kuti si ulamuliro wa adani a mpingo wokha umene udzachotsedwa, koma Mesiya ndi abwenzi ake onse adzalandira ulamuliro monga mwa mau apa Afilipi 2:9-11, amene akuti, “Mwa ichinso Mulungu anamkweza Iye, nampatsa dzina limene liposa mayina onse, kuti m’dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m’mwamba ndi za padziko, ndi zapansi pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali ambuye, kuchitira ulemu Mulungu Atate.” Kutsindika kunena kuti Ambuye Yesu analandira ulamuliro ndi ufumu kuchokera kwa Iye, amene ali ndi ufulu wonse wopereka kwa Iye, popanda munthu wina aliyense kumufunsa kuti uchitiranjire?Tere ichi, ndichimene Ambuye Yesu adanenetsamupemphero lake pa Luka 11:2, pamene anati, “M’mene mupempheraneni, Atate, Dzina lanu liyeretsedwe; Ufumu wanu

udzedze.”Apa, anali kunena kuti Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wokhawo umene ulibe malire. Kunena kuti ngakhale anthu ena akhala akukhazikitsa maufumu awo, kapena kuyesera kukhala ndi ufumu waukulu, koma chodziwika ndi chakuti, anthu onse ndi mitundu yonse yapa dziko lapansi, ayenera kulemekeza ndi kukhala pansi paulamuliro wa Mulungu. Kutsindika kuti munthu wina aliyense ali pansi pa ulamuliro wa Mulungu, kaya akuchita mobvomereza kapena mwakukhala kapolo pansi paulamuliro wake. Mwanjira ina tikunena kuti kudzera kumbali zonse ziwirizi, maufumu onse a dziko lapansi ndiwo maufumu a Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo mau onsewa akulinga pakuti, Ufumu wa Mulungu ndiwo Ufumu wamuyaya, umene sudzatha, kotero kuti palibenso amene angalowepaufumu umenewu. Komanso palibe mdani amene anganene kuti ukathaalowapo iye. Tikunena kuti ngakhale makoma aku Gahena, kaya mphamvu za kumidima ndi ulamuliro wake, sadzakhoza kupambana mu Ufumu uwu. Kutanthauza kuti mpingo wa Ambuye udzakhalabe chikhalire wosathyoka kufikira kunthawi za muyaya. Ndiye mau onsewa akungotsimikiza za kubweranso kwa Ambuye pamene

fanololidzathyoka ndi mwalawosemedwa wopanda manja  
(Chibv.19:11-19).

15.Koma ine Danieli, Mzimu wanga unalaswa m’kati mwa thupi  
langa ndi masomphenya a m’mtima mwanga anandibvuta.

Tsopano Danieli wangomaliza kumene kuona matanthauzo a  
magawo a masomphenya, ndiye pano akuona tanthauzo la  
masomphenya onse. Izi, ndizinthu zomwe Danieli adaona zomwe  
pakuzilingalirazinamukhudza kotero kuti Mzimu wake unalaswa  
m’kati mwa thupi lake. Kutanthauza kuti Danieli anachititsa  
mantha kwambiri, ndipoanasowa mtendere. Nkhani ikuti Danieli  
anachita mantha osati chifukwa sanabvetse tanthauzo la  
masomphenyawo ayi, popeza pa Danieli 7:28, akunenetsa kuti iye  
anachita mantha chifukwa cha maganizo ake. Kunena kuti mngelo  
wa Mulungu anamufotokonzera bwino ndipo anamvetsa, komanso  
kuti anasowa mtendere chifukwa chakuona mwana wa munthu ndi  
ulemerero wa ufumu wake ayi. Iye, anasauka kwambiri chifukwa  
cha zirombo zinayi maka-makachirombochotsiriza cha chinayi ndi  
nyanga yake yaying’ono. Tsono tanthauzo la masomphenya ndi  
chilango chomwe chinaonetsedwa kwa iye ndi zomwe anthu a

Mulungu ayenera kuyendamo ndi kufika muufumu wa Mulungu wamuyaya.

16.Ndinayandikirakwa wina wa iwo akuimako ndi kumfunsa za choonadi za ichi chonse. Ndipo ananena nane, nandidziwitsa kumasulira kwake kwazinthuzi.

Danieli ataona kuti sanali kuzimvetsa zinthu zina, anapita kwa m'modzi wa angelo amene anali ndi mwana wa munthu muulemerero wake, ndi kumufunsa choonadi ndi tanthauzo la zinthu zomwe adazionazo. Ndiye tikunena kuti ndichinthu chofunika kumvetsa ndi kutenga tanthauzo la zinthu zomwe tikumva kuchokera kwa Mulungu. Tsono iwo amene afuna kudziwa, ayenera kufunsa ndi chikhulupiriro chonse mwa njira ya kupemphera. Kutsindika kunena kuti inu ndi ine, ngati wokhulupirira sitienera kuchita manyazi kufunsirakwa wina aliyense amene tiyembekezakupezako chidziwitso choona, makamaka kwa iwo amene ali wokhwima m'moyo wauzimu. Tere, ndichifukwa chake Danieli akunena kuti atakafunsakwa mngelo, anauzidwa tanthauzo la masomphenya ndi cholinga chomwe anaperekedwera.

Wokondedwa anzanga apaulendo mwa mau awa, tikunenetsa kuti Mulungu alindiangelo amene ayenera kupereka Uthenga wachoonadi kwa anthu ake. Tere pa Chibvumbulutso 1:1, pali mau akuti, “Chibvumbulutso cha Yesu Kristu, chimene Mulungu anamvumbulutsiraachionetsere akapolo ake, ndicho cha izi ziyenera kuchitika posachedwa; ndipo potuma mwa mngelo wake anazindikiritsa izi kwa kapolo wake Yohane.”

17.Zirombo zazikuru izi zinayi ndizo mafumu anayi amene adzauka pa dziko lapansi.

Danieli wakhudzidwa ndi masomphenya a zirombo ndipo wapita kwa mngelo amene wadza ndi mwana wa munthu, kukafunsitsa za tanthauzo la masomphenyawo. Ndipo mngelo anamuuza mwatsatane-tsatane za chinthucho.Tsono mngelo akuti zirombo zomwe zinaonekazo, zikuimira mafumu ndi ufumu wawo, umene udzauka pa dziko lapansi, monga momwe zirombozozinaturukam’nyanja. Uwu, ndiwo ufumu wa m'dziko lapansi, popeza unaturukakunthaka, kotero kuti udzabwereransokunthakakomweko.

Tsono Danieli anamvetsa tanthauzo la zirombo zitatu zija, koma pano afunitsitsaatadziwa tanthauzo la chirombochachinayi, popeza ichochi, ndicho chosiyana ndi zirombo zina zonse. Ichi, ndicho chirombo chomwe chinachititsa mantha kwambiri chifukwa cha mphamvu zake, popeza chinathyola zinthu zambiri. Tere, ndichifukwa chimenechi, chomwe chinapangitsa mantha ndi kusautsa Danieli. Danieli anafunitsitsa atadziwa tanthauzo la nyangayaing'ono yomwe inali ndi maso. Tsono nyanga iyi, ndiyo inali kuthyola ndi kuphwanya zinthu monga mbiya. Ndiye Danieli anali ndi funso lakuti, kodi Yehova adzataya anthu ake? Kodi adzalora adani kuzunza anthu ake? Kodi nyanga yake ndi iti, yomwe idzasautsa ana a Mulungu? Ndiye pakali pano tiyenera kudziwa kuti mfumu iliyonse pamafumuanayiwa, ikuimira ufumu. Awa, ndi mafumu monga Nebukadnezara, Alexander, Antiochus, ndi wokana Kristu.

18. Koma opatulika a Wamwambamwamba adzalandira ufumuwu ndi kukhala nawo ufumu kosatha, ku nthawi zomkamuyaya.

Nkhani pano ikuti, opatulika a Wamwambamwamba, adzalandira ufumuwu ndi kukhala nawo ufumu kosatha, ku nthawi

zomkamuyaya. Poyamba ndikoyenera kuti tidziwe opatulikawa ndiwo ayani? Tikaonetsetsa mu chapter chino, tipeza kuti liwu lakuti, “opatulika” likutchulidwa kasanu mu verse 21, 22, 25 ndi 27. Komanso likuonekanso mu Danieli 8:24, momwe akuti, “Ndi mphamvu yake idzakhala yaikuru, koma si mphamvu yake yake ayi, ndidzaonongamodabwiza, nidzakuzika ndi kuchita ndi kuononga amphamvuwo ndi anthu opatulikawo.” Tsono pamene tiwerenga m’Chipangano Chatsopano pa Aroma 1:7, akufotokonza kuti opatulika kapena woyera mtima, ndiwo anthu ochimwa amene anasandutsidwa woyera chifukwa cha chikhulupiriro chawo mwa Kristu. Koma m’Chipangano Chakale pa Eksodo 19:6, akunena kuti mtundu wa Israyeli ndiwo wopatulika. Ndiye tikunena kuti m’buku la Danieli wopatulikawa, ndiwo mtundu wa Israyeli amene anakhulupirira Yehova. Ndikunena mau amenewa chifukwa mpingo, sukuonetsedwapenapaliponse m’Chipangano Chakale.

Ndiye Danieli akunena kuti anthu opatulikawa ndiwo amene adzatenga ulamuliro wapa dziko lonse lapansi kufikira nthawi zamuyaya. Ichi, ndicho cholinga chachikulu cha masomphenya amenewa, kotero kuti panali cholinga chakuti wokhulupirirawo,

aike maso awo pachimenechi. Kutanthauza kuti zinthu zonse zomwe zinali kuchitika m'mbuyomo, zinali kukonzekeretsa kukwaniritsidwa kwa cholinga chimenechi. Nkhani iyi, ikuona kutsogolo kuti anthu onse wokhulupirira, amene ndiwo opatulika, oopa Mulungu, adzatenga ulamuliro paufumuwa dziko lonse lapansi. Uwu, ndiwo ufumu umene sudzatha komanso sipadzabwera wina pambuyo pake ayi. Koma sitikunena kuti padziko lapansi padzakhala ufumu wamuyaya ayi. Tikunena kuti Ambuye Yesu Kristu adzakhazikitsa ufumu wawo padziko lapansi kwa zaka chikwi, apa ndipo padzakhala ufumu wachilungamo pansi pano. Koma chilungamo chimenechi chidzapitiliramufumuwa m'Mwamba womwe udzakhala kwamuyaya. Kodi inu mwakonzeka kukhala pagulu la anthu opatulika?

19. Pamenepo ndimafuna kudziwa choonadi cha chirombochachinayi chija chidasiyana nazo zonsezi, choopsa chopambana, mano ake a chitsulo, ndi makadabo ake a mkuwa, chimene chidalusa ndi kuphwanya ndi kuponderezazotsala ndi mapazi ake.

20.Ndi za nyanga khumi zinali pamutu pake ndi nyanga yina idaphukayi, imene zidagwa zitanu patsogolo pake; nyangayoidali ndi maso ndi pakamwa pakunena zazikuru, imene maonekedwe ake anaposazinzake.

Tsono Danieli analibe bvuto ndi kumasulira kwa zirombo zitanu ndi mafumu amene zirombozozimaimira. Koma anabvutika kwambiri mumtima ndi chirombochachinayi.Ichi, ndicho chinali chochititsa chidwi popeza chinali kuoneka choopsa kwambiri malinga ndi momwe chimaonekera. Taonani nyanga zake zinali zambiri, ndipo kumerakwanyangayaing'ono, kunali koopseza kwambiri. Komanso chiweruzo chomwe chinaperekedwa pa chirombochichinali chotsimikizika ndithu. Ndiye panalinso masomphenya a mwana wa munthu, amene anadza kudzatenga ulamuliro wa ufumu wa dziko lapansi.

Ndiye tanthauzo la masomphenyawa likuti nyanga khumi zikuimira mafumu khumi.Ndipo nyangayaing'ono ndiyo mfumu imene idzaphuka pakati pa mafumu awa, ndipo idzagonjetsa mafumu atatu ndipo idzachitira mwano dzina la Mulungu. Uyu, ndiye mfumu amene adzalankhula mau akuru kwa Mulungu

nanyozerachilungamo cha Mulungu. Iyeyu, adzazunza wokhulupirira ake a Mulungu. Ichi, ndicho cholinga cha satana kuzunza ana a Mulungu. Kutsimikiza kuti nyangayaing'ono iyi, ndiye wotsutsa kapena wokana Kristu, malinga ndi 2 Atesalonika 2:3-4, pamene pali mau akuti, “Munthu asakunyengenikonseko; kuti silifika, koma chiyambechifikechipatukocho, nabvumbulutsike munthu wosayeruzika, mwana wa chionongeko, amene atsutsana nazo, nadzikuza pa zonse zotchedwa Mulungu, zopembedzeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu.”

21. Ndinapenya ndipo nyanga yomweyo inachita nkondo ndi opatulikawo, niwalaka, mpaka inadza nkhalamba ya kale lomwe.

Tsono pano ndikoyenera kunena kuti Roma udzakhalanso ufumu wamphamvu padziko lonse lapansi, pansi pa ulamuliro wawokana Kristu. Wokana Kristu ndiye amene ali ndi mau ochitira Mulungu mwano komanso adzazuza ana a Mulungu. Ichi, ndicho chimene tikuwerenga pa chibvumbulutso 13:7, pamene pali mau akuti, “Ndipo anachipatsa icho, kuchita nkondo ndi woyera mtima ndi

kuwalaka; ndipo anachipatsaulamuliro wa pa pfuko liri lonse ndi anthu ndi manenedwe ndi mitundu.” Ulamuliro uwu, udzaperekedwakwa kanthawi kochepa kumapeto a nthawi yachibvuto chachikuru. Koma mpingo udzakhalautachotsedwa kale, chibvuto chachikuru chisanafike.

Tsono Pachifukwa chimenechi, tikuona kuti Aroma ndiwo anthu amene akhala akuchita nkondo m'moyo mwawo. Ndipo lero lino ku Europe, Asia ndi kumpoto kwa Africa (Aigupto), ndimaiko momwe muli zizindikiro zonse za nkondo ngakhale akutchula mtendere. Ndiye nkhani ikuti ufumu wa Aroma udzasonkhanitsidwanso pansi pautsogoleri wa wokana Kristu. Iyeyu adzakhala pampando waulamuliro kotero kuti adzalankhula mau ochitira Mulungu mwano (Chibv. 13:6).

Munthu uyu, adzabweramonyenga kwambiri, monga Bishop Fulton J. Sheen adanena kuti, “Wotsutsa Kristu adzabweramodzibisa monga munthu wochitira anthu chifundo. Iyeyu adzalankhula mtendere, kutukuka ndi kukhala ndi chuma chambiri, zomwe ziri njira zokwaniritsa cholinga chake. Uyu, ndiye munthu amene adzafalitsa nzeru yakuti anthu sadzapeza mtendere pokha-pokha

akhale m'bungwe limodzi.”Tsono lero mukaonetsetsa, mupeza kuti Europe akupita ku nzeru yosonkhana pamodzi. Ichi, ndichikonzerochikubwerakwa wokana Kristu.

22.Ndi mlandu unakomeraopatulika a Wamwambamwamba, nifika nthawi yakuti ufumu unali wawo waopatulikawo.

Ndime ino ikunena za kusintha kwa ulamuliro. Kutanthauza kuti ndi Yesu Kristu yekha amene adzagonjetsa wokana Kristu ndi ufumu wake. Kutsimikiza kuti nthawi ikudza pomwe Mulungu adzatenga ulamuliro wadzikoli.Apa ndipo pamene wokana Kristu adzagonjetsedwa, ndipo chipembedzo choona chidzakhazikika ndi kulamula miyoyo ya anthu ambiri. Kutsindika kuti iyi ndi nthawi yomwe ufumu wa Mesiya udzakhazikitsidwa mwanjira yofalitsa Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu Kristu. Mulungu nthawi iyi, adzaweruzamolungama ndipo adzagwiritsa ntchito Mwana wa munthu pamodzi ndi wopatulika.

23.Anatero, chirombochachinayi ndicho ufumu wachinayi pa dziko lapansi, umene udzasiyana nawo maufumu onse, nudzalusira dziko lonse lapansi, nudzalipondereza ndi kuliphwanya.

Tsono nkhani ikunena kuti padzakhala ufumu wachinayi, umene ukuonetsedwa ndi chirombochachinayi. Ufumu uwu, udzalowa m'malo mwa maufumu atatu aja, momwe mkango, chimbalangondo ndi nyalugwe zikuimira. Uwu, ndi ufumu wamphamvu ndipo udzaononga maufumu ena onse ndiye kuchoka muufumu uwu, mudzaturuka ufumu khumi, umene udzakhala ndi mafumu khuminsu. Ndiye mkati mwaufumuwachinayi mudzaturuka mfumu ina yomwe idzaononga maufumu atatu ena. Uwu, ndiwo ufumu wa Roma, umene udzakhalapobe kufikira kubwera kwa Kristu kwachiwiri.

Wokondedwa anzanga apaulendo tiyeni titsirize ndi mau akuti, ufumu wa Aroma ndiwo wamphamvu kotero kuti ndi ufumu wa Mesiya wokha umene udzaononga ufumu umenewu. Ichi, ndicho chiyembekezo cha wokhulupirira kuti Kristu akudza kudzathunzitsa mitima yawo. Kodi inu mulinacho chiyembekezo chimenechi?

Lero tilekeza pano. Ndipo timasanthula Danieli 7:13-23, momwe timaunika za tanthauzo la zirombo zinayi.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!

